# MATENDA A CHISAKA CHA NTHOCHI (BANANA BUNCHY TOP DISEASE -BBTD)



Matenda a chisaka cha nthochi

© DARS

**Chisaka ndi matenda amodzi oopsa anthochi amene amayambitsidwa ndi kachirombo kosaoneka ndi maso kotchedwa Vayilasi (virus).**

## MOMWE MATENDAWA AMAFALIKIRA

- **Matendawa amafalitsidwa ndi nsabwe za mu nthochi.**
- **kubzala nthochi zogwidwa kale ndi matendawa.**
- **kugwilitsa ntchito zipangizo zimene zagwira kale ntchito pa nthochi yamatenda.**
- **kubzala nthochi pamalo pamene pali mbiri yamatendawa.**

## ZIZINDIKIRO ZA CHISAKA CHA NTHOCHI

Nthochi imakwinimbira/ imanyentchera Masamba





amakhala okwinimbira, osongoka komanso ounjikana ndipo sachedwa kung'ambika

Nthochi sibereka, koma ikabereka zipatso zimakhala zazing'ono, zochepa komanso zosaoneka bwino

Some elements adopted © CABI / PLANTWISE / PLANTVILLAGE

**KUTHANA NDI CHISAKA CHA NTHOCHI**

**Yendelani munda wa nthochi pafupipafupi**

- **Gwiritsani ntchito masakazi/ana a nthochi/Mphukira amene alibe matenda;**
    - **Ochokera ku malo opanda mbiri yamatenda**
    - **Ogulidwa kumalo amene amapangidwa ndi njira zamakono (tissue-culture)**
- **Bzalani nthochi pa mtunda wa mamita 100 kuchokera m'minda ya nthochi ya kale**
- **Bzalani nthochi zopilira kumatendawa**
- **Pewani kugwilitsa ntchito zipangizo zimene zagwira ntchito pa nthochi ya matendawa pokhapokha mutazipopera mankhwala kapena kuziwaula ndi moto (sterilization)**
- **Zulani ndi kuwotcha nthochi zomwe zagwidwa ndi matenda, siyani munda wanu kwa pakati pa miyezi 6 ndi zaka 2 musanabzalenso nthochi**
- **Palirani m'munda kuti muchepetse malo omwe nsabwe zingabisale**
- **Chotsani duwa pa mkoko wa nthochi kuti muchepetse nsabwe**
- **Poperani mankhwala kuti muchepetse nsabwe m'munda wa nthochi**





**Nsabwe zofalitsa chisaka cha nthochi**

© DARS | M FLPA / FLICKER/SCOT NELSON

**Dziwitsani alangizi a zamalimidwe ngati mwaona zizindikiro za chisaka m'munda mwanu**

**Malawi**

**Created/Edited on August 14, 2025**

© MINISTRY OF AGRICULTURE, MADIPHS PROJECT,
CC BY-NC-SA 4.0 LICENCE